# KUCHOTSA MIMBA NDI MAKHAWALA A MISOPULOSITO

## KUDALILIKA KWA MAKHWALAWA

Njira yochotsa mimba pogwilitsa ntchito makhwala a Misoprostol ndiyodalilika, pa amayi khumi omwe agwiritsa ntchito misoprostol kuchotsa mimba, Amayi asanu ndi anayi mimba zawo zimachoka popanda vuto lilironse.

## NGATI MAKHWALA SANAGWIRE NTCHITO TITANI

**Tiyenera kumwanso makhwala misoprostol kapene kuchotsa pogwilitsa njira kuchipatala.** Ndipovuta kusunga mimba yomwe yalephereka kuchoka mutamwa misoprostol chifukwa mwana sakhalanso ndi moyo.

## WAS MY ABORTION SUCCESSFUL?

**Ngakhale Mayi ali ndi chitsimikizo chonse kuti mimba yachoka komabe ayenera kukayezetsa kuti atsimikize kuti mimba inachok adi ayenera kukayezetsa patahta masabata atatu kapene anayi.**

Ngati mayi wamwa mankhwala ochotsera mimba ndipo wataya magazi ochepa kwambiri komanso akumva zizindikiro zakuti mimbayo ikadalipobe, ayenera kuyezetsa kuti adziwe kuti mimbayo ikadalipo kapena yachoka. Ngati wapeza kuti mimbayo sinachoke, ayenera kumwanso mankhwala ochotsela mimbayo potsata ndondomeko zonse monga anachitila poyamba paja.

## MIMBA IKACHOKA

- Mayi akamaliza kuchotsa mimba magazi amakhala akutuluka kumaliseche kuyambira sabata imodzi mpaka masabata atatu. Koma zimasiyana amayi ena amapanga sabata imodzi ena mpaka masabata atatu.
- Amayi akulangizidwa kuti pamene amaliza kuchotsa mimba sakuyenera kulowetsa katnthu kena kalikonse kulaliseche, kusamba komanso kugonana ndi mwamuna mpaka patatha masiku awiri chichotseleni mimba.
- **Kodi mayi akhoza kutenga mimba ina atangomaliza kuchotsa mimba!** Mayi akhonza kutenga mimba atamaliza kuchotsa mimba ina ngati agonana ndi mwamuna asanatenge makhwala olera.



## KODI MISOPULOSITO NDICHIYANI

MISOPULOSITO ndi makhwala omwe amagwilitsidwa pa dziko lonse la pansi kwa amayi omwe akufuna kuchotsa mimba komanso amachiza matenda a zilonda za mmimba. Makhwsalaw-a amagulitsidwa mmalo ogulitsa makhwala mma pharmacy ndi maina osiyana siyana monga Cytotec, Isovent, Misoclear, Misofem, Cyrux kapena Tomispral. Maiko ambiri mu Africa makhwalawa amagwilitsidwa ntchito pofuna kuchepetsa kutayika kwa magazi kwa amayi a pakati pobeleka mwana

## CONTACTS


Women HelpWomen
WEB: HTTPS://WOMENHELP.ORG/ EMAIL: INFO@WOMENHELP.ORG
TWITTER: @WOMENHELPORG FACEBOOK: WOMENHELPWOMENINTERNATIONAL
MAMA Network: Mobilizing Activists around Medical Abortion (MAMA).
WEB: WWW.MAMANETWORK.ORG
Trust for Indigenous Culture and Health (TICAH)
WEB: WWW.TICAHEALTH.ORG EMAIL: LISTENING@TICAHEALTH.ORG
TWITTER: @YOURAUNTYJANE FACEBOOK: AUNTY JANE HOTLINE

CENTRE FOR SOCIAL CONCERN AND DEVELOPMENT (CESOCODE)
ADIRESI: P.O BOX 218, LUNZU, MALAWI
TELEFONI: +265 999458907
EMAIL: CESOCODE@YAHOO.COM


women help women

## KODI MISOPULOSITO AMAGWILITSIDWA NTCHITO BWANJI

Misopulosoto amagwilitsidwa ntchito pa njira izi, kuchotsa mimba komanso kupititsa pachabe (kuthandiza kutsilizitsa ngati mayi akuchotsa mimba). Kuchepetsa kutaya kwa magazi ochulupa pamen mayi wa mimba pobereka komanso kuchiza zilonda za mmimba zomwe zimatchedwa kuti ma ansazi.

## KODI MISOPROSTOL AMAGWIRA NTCHITO BWANJI?

Misoprostol amapangitsa chibelekero kuti chinyale kenako chimadzafewa zomwe zimapangitsa kuti njira ya chibelekero itseguke ndikupangitsa kuti mimba ichoke ndi kuti Mayi achite ngati wapita pachabe.

## KODI MISOPROSTOL ANGAGWILITSIDWE NTCHITO POCHOTSA MIMBA YA MASABATA NGATI?

Mankhwalawa angachotse mimba yomwe sinaposele masabata khumi ndi awiri kuyambira kuwerengera tsiku lomaliza kusamba.

## NDONDOMEKO YA MMENE TINGATSATE POCHOTSA MIMBA POGWILITSA NTCHITO MAKWALAWA

Mayi ayenera kumwa mapilisi okwana khumi ndi awiri (12) omwe amamwedwa katatu pa mapilisi anayi pakatha maola zitatu motsatizana.

Tengani mapilisi anayi ikani mkamwa kunsi kwa lilime yembekezani mpaka mphindi makumi atatu azisungumuka inu muzimeza malovu.

Pakatha maola atatu ikaninso mapilisi ena anayi kunsi kwa lilime ndikudiila mphindi makumi atatu ndipo mapilisi azisungunuka ndi malovu a mkamwa inu muzimeza malovuwo.

Pakathanso maola atatu ikaninso mapilisi ena anayi kinsi kwa lilime awiri mbari ina awirinso mbari ina yembekezani kwa mphindi makumi atatu mpaka onse atasungunuka inu muzikhala mukumeza malovu.

**Ngati kuchotsa mimba sikunachitike patapita ma ola okwana atatu mutamwa mwankhwalawa,muyeneranso kumwa Misoprostol kutsatila ndondomeko yoyenera mpaka mimba itachoka.**

## ZOTSATILA ZAKE MUKAMWA MAKHWALAWA

| | | |
|---|---|---|
| Kumaliseche kwanu kumayamba kutuluka magazi owundana komanso ofewa osiyana ndi magazi omwe amatuluka mukamapanga msambo wamwezi. | Kwa Amayi ochuluka mimba imachoka pakatha ma ola 24 atamwa makhwala | Mimba ikakhala ya masabata ochuluka magazi ake amakhala oilmbans kwambiri. |

Makhwala ochepetsa ululu ayenera kumwedwa kumayambiriro pamene tikumwa gawo loyamba la Misoprostol. **Ibuprofen** ndi makhawala a mphamvu pofuna kuchepetsa ululu. Komanso tikhonza kumwa **paracetamol** pofunanso kuchepetsanso ululuwo.



## ZIZINDIKIRO ZAZIKULU ZIKULU

Mu maola makumi awiri ndi ndi mphambu zinayi pamene wamwa Misopulosito mumaona zizindikilo izi nseru, kusamza, kutsekula mmimba, kutentha kwa thupi, litsipa komanso chizungulire. Zizindikiro zimenezi ndizosaopya komanso zimatha pakapita nthawi yochepa.

## ZIZINDIKIRO ZOTICHENJEZA

- Kutaya magazi ochuluka pamka kugwilitsa ntchito ma padi atatu pa ola limodzi kwa maola awiri kapene atatu
- Kutentha thupi kopyola 38 kapena 39 gidiri popyola maola makumi awirir ndi mphambu zinayi
- Kuphwanya kwa thupi kosaleka ngakhale mutamwa panadol patatha masiku ochepa chimwereni misopolosito
- Fungo lonunkha komanso kutuluka mafinya ku maliseche kwanu

## ZOMWE NDINGACHITE ULULU UKAMAPITILIRA

**Kupita mwansanga kuchipatala kukakumana ndi dotokala**

Pamene mwapita ku chipatala kafotokozeni kuti mwapita pachabe ndipo dotolo akakupatsani chithangato choyenera. Pamene mwachotsa mimba ndi makhwala a mifepristone ndi misoprostol sipakhala kusiyanitsa ndikupita pachabe.